

“Pakuti maganizo anga sali maganizo anu, ngakhale njira zanu siziri njira zanga, ati Yehova” (Yesaya 55:8).

16 Amai achikhristu kuti akapembedze ndi kutamanda Mulungu. “Ndidzayimbira Yehova m'moyo mwanga: Ndidzayimbira Mulungu wanga zomlemekeza pokhala ndiripo” (Masalmo 104:33).

17 Amai, kuti akakondweretsa Mulungu kudzera m'malankhulidwe awo, malingaliro awo, komanso zochita zawo.

18 Amai, kuti akakhale a machawi kuuza ena zimene Mulungu wawachitira. “Pakuti sitingathe ife kuleka kulankhula zimene tinazona ndi kuzimva” (Machitidwe 4:20)

19 Amai kuti akawonetsera ndi kuchitira umboni za chikondi cha m'moyo wawo wa tsiku ndi tsiku. “Ndipo masiku onse, m'Kacisi ndi m'nyumba, sanaleka kuphunzitsa ndi kulalikira Kristu Yesu” (Machitidwe 5:42).

20 Amai kuti akalankhula “choonadi mchikondi” (Aefeso 4:15) ndi kulora kuti Mzimu Woyera “adzatsutsa dziko lapansi za macimo, ndi za cilungamo, ndi za ciwuziro” (Yohane 16:8).

21 Akhristu, kuti akalalikira kuti uthenga wakuti “Pakuti Mulungu anakonda dziko lapansi kotero, kuti anapatsa Mwana wace wobadwa yekha, kuti yense wakukhulupirira iye asatayike, koma akhale nao moyo wosatha” (Yohane 3:16).

22 Akhristu kuti akatha kuchenjeza ena mwachikondi, powauza kuti “Wokhulupirira iye saweruzidwa; wosakhulupira waweruzidwa ngakhale tsopano, cifukwa sanakhulupirira dzina la Mwana wobadwa yekha wa Mulungu” (Yohane 3:18).

23 Amayi amene chikhalidwe ndi zikhulupiliro zawo zimawalepheretsa kumva uthenga wa chikondi vha Mulungu komanso chiyembekezo chimene angapeze mwa Yesu Khristu. Ambiri akumamvetsera mawu a Mulungu kudzera pa ma pologalamu a pa wailesi ndi kudziwa zambiri za Yesu.

24 Amai kuti akakondwerera ndi uthenga wa Khrisimisi, uthenga wa chiyembekezo, chimwemwe komanso mtendere, pouza ena zimene Mulungu wachita m'miyoyo yawo.

25 Iwo amene akukhala mosowa chiyembekezo, kuti akapeza chiyembekezo mwa Yesu Khristu. Tipemphere kuti iwo akamva za mphatso yopambana ya chipulumutso cha Mulungu mwa Yesu Khristu. “Ndipo mngelo anati kwa iwo, Musaope; pakuti onani, ndikuuzani inu uthenga wabwino wa cikondwero cacikuru, cimene cidzakhala kwa anthu onse; pakuti wakubadwirani inu lero, m'mudzi wa Davide, Mpulumutsi, amene ali Kristu Ambuye” (Luka 2:10-11).

26 Amai amene akumvera ma pologalamu a Mayi wa Chiyembekezo, kuyendera nyumba za Hannah, kapenanso kutengapo mbali pa magulu a mapemphero. Tipemphere Ambuye kuti asunthe mitima yawo kuti akathe kumvetsetsa choonadi cha uthenga wabwino, ndi kukhala pa ubale ndi Yesu Khristu.

27 Ma pologalamu a Mayi wa Chiyembekezo, kuti akalimbikitsa amayi amene ataya chiyembekezo, kupereka mphamvu kwa iwo amene ali ofooka, kukweza akugwa, kupereka chilimbikitso kwa amphamvu kuti iwo akathe kuthandiza amene ali osowa; kulimbikitsa omvera kuti akayendebe ndi Ambuye; komanso kukumbutsa iwo amene ali osiyidwa kuti sali okha.

28 Amai kuti akakhale okonzeka kusintha zochita zawo, ndondomeko za moyo wawo, maubwenzi awo, komanso chilli chonse chimene chikulepheretsa kuti iwo asatsate chifuniro cha Mulungu. “Mundidziwitse njira zanu, Yehova; mundiphunzitse mayendedwe anu. Munditsogolere m'coonadi canu, ndipo mundiphunzitse; pakuti Inu ndinu Mulungu wa cipulumutso canga; Inu ndikuyembekezerani tsiku lonse” (Masalmo 25:4-5).

29 Amai kuti akatenga nthawi kudziwa malingaliro a Mulungu, chikhalidwe chake, komanso njira zake pamene akusanthula Malemba. Tipemphere kuti pamene akuphunzira zambiri za Mulungu, iwo akakhudzika ndi zinthu zimene zimakhudza mtima wa Mulungu, komanso kukondwa ndi zimene zimam'kondweretsa.

30 Amai amene akukumana ndi nyengo zovuta monga umphawi, kutha kwa banja, kusakhulupilika kwa m'banja, mchitidwe ogulutsa matupi, kapenanso HIV ndi Aids. Tipemphere kuti iwo akalora Mulungu kuti awakute ndi chilungamo chake.

31 Chitsogozo cha Mulungu m'chaka cha tsopano kwa Amai a Chiyembekezo a TWR, pamene akufalitsa chiyembekezo ndi machiritso kwa amai padziko lonse ndi m'mibadwo yosiyana siyana.


Listen to Project Hannah *Women of Hope* radio programmes on:

- TWR Africa (*DSN 855*) or TWR Africa2 Satellite Service (*SES-5*)
- Project Hannah App (*Android and iPhone*)
- www.projecthannah.org - “LISTEN NOW”

Pali pulogilamu mu Chingerezi yotchedwa *Women of Hope* yomwe ikuulutsidwa mu zilankhulo zopitilira 65 komanso mndandanda wa mapemphero mu ziyankhulo 85 kuphatikizapo Chichewa.

Kupempherera

Amayi
Kuti Apeze
Moyo Wa
Muyaya



Prayer Calendar
December 2016

Chichewa



Moyo wa padziko pano ndi wa nthawi yochepa. Koma moyo wa muyaya ndi wa nthawi yaitali kwambiri. Chinthu chimodzi ndi chodziwikiratu: aliyense adzamwalira tsiku lina. Amai kulikonse amakhala otanganidwa ndi moyo wa tsiku ndi tsiku (kukonza chakudya, kusankha zovala, komanso kukonza pakhomu). Komatu kukonzekera moyo wa muyaya ndiye chofunika koposa, ngakhale kuti anthu samalingalira izi motere.

Mkaganizidwe ka chikhrisitu, muyaya umaphatikizapo Utatu Woyera wamuyaya Mulungu Tate, Mwana ndi Mzimu Woyera). Mulungu analenga zonse ndipo amazionetsera yekha mu chilengedwe Chake. Munthu akamwalira, mzimu wamunthuyo umakhalabe ndi moyo kumwamba kapena ku gehena.

Anthu amasankha kumukana Mulungu, kubweretsa uchimo mudziko lapansi. Chifukwa choti Mulungu si wongoyera kokha komanso ndi wachifundo ndi wachikondi, anavala umunthu muumunthu wa Yesu Khristu (Mwana) kukhala moyo wopanda uchimo pa dziko lapansi ndi kufa ngati dipo la uchimo wathu. Tikavomera mphatso ya Mulungu ya chipulumutso ku machimo kudzera mu kufa ndi kuuka kwa Yesu, Mulungu amasankha kusaonanso tchimo lathu ndi kuona Yesu monga woyera mmalo mwathu. Chifukwa cha Yesu, timakhala mmoyo wobwezeretsedwa muubwenzi ndi Mulungu tsiku ndi tsiku.

Mulungu Mzimu Woyera amakhala mwa aliyense wotsatira Yesu moonadi. Pamene tikanali pa dziko lapansi, Mawu a Mulungu (Malemba) ndi Mzimu Woyera amatiphunzitsa njira za Mulungu ndi kutithandizira kukhala otsatira enieni a Yesu. Moyo padziko pano ukatha, Akhrisitu nthawi yomweyo amakhala pamaso pa Mulungu mpaka ku nthawi zosatha kumwamba.

Mulungu amakonda munthu aliyense ndipo amakhumba kuti aliyense akakhale naye mu muyaya. Mulungu amalambulira akhrisitu kukhala mboni, kuwauza ena za chikondi chake ndi mmene angabwezeretsere ubale wawo ndi lye kudzera mwa mphatso ya chipulumutso ya Yesu. Moyo ndi waufupi, ndiye auzeni msanga.

Chonde tipempherere...

1 Amai kuti adziwe kuti Mulungu analenga zinthu zones, kuphatikizapo iwowo, kuti akaonetse mphamvu ndi ulemerero wake. Chidziwitso ichi, chiwatsogolere kuti akazindikire kuti Mulungu ndi woyenera kulandira matamando awo. “Muyenera inu, Ambuye wathu, ndi Mulungu wathu, kulandira ulemerero ndi ulemu ndi mphamvu; cifukwa mudalenga zonse, ndipo mwa cifuniro canu zinakhala, nizinalengedwa.” (Chivumbulutso 4:11)

2 Amai kuti amvetsetse kuti Mulungu amaziwonetsera yekha kwa aliyense kudzera m’chilengedwe chake. “Zakumwamba zimalalikira ulemerero wa Mulungu; Ndipo thambo lionetsa nchito ya manja ace” (Masalmo 19:1). “Pakuti cilengedwere dziko lapansi zaoneka bwino zosaoneka zace ndizo mphamvu yace yosatha ndi umulungu wace; popeza zazindikirika ndi zinthu zolengedwa, kuti iwo adzakhale opanda mau akuwiringula” (Aroma 1:20).

3 Amai kuti adziwe kuti Mulungu amawakonda ndipo kuti akufuna kuti iwo akhale gawo la banja lake kwa muyaya, kuti potero, iwo akalandire cholowa cha mu ufumu wa Mulungu. “Wodalitsika Mulungu ndiye Atate wa Ambuye wathu Yesu Kristu, iye amene, monga mwa cifundo cace cacikuru, anatibalanso ku ciyembekezo ca moyo, mwa kuuka kwa akufa kwa Yesu Kristu; Akuti tilandire colowa cosabvunda ndi cosadetsa ndi cosafota, cosungikira m’Mwamba inu” (1 Petro 1:3-4).

4 Amai kuti amvetsetse kuti onse anachimwa ndipo kuti uchimo umawalekanitso iwo ndi Mulungu. “Pakuti onse anacimwa, naperewera pa ulemerero wa Mulungu” (Aroma 3:23). “Pakuti mphotho yace ya ucimo ndi imfa; koma mphatso yaulere ya Mulungu ndiyo moyo wosatha wa mwa Kristu Yesu Ambuye wathu” (Aroma 6:23).

5 Amai kuti amvetsetse kuti Mulungu amadana ndi tchimo, ndipo kuti uchimo onse nmdi otsutsana ndi Mulungu. “Pa Inu, Inu nokha, ndinacimwa, ndipo ndinacita coipaco pamaso panu: Kuti mukhale wolungama pakulankhula Inu, mukhalenso woyera pa kuweruza kwanu” (Masalmo 51:4).

6 Amai kuti amvetsetse kuti Mulungu amakonda aliyense wa ife, koteru kuti anabwera ku dziko lapansi m’maonekedwe a umunthu, mwa Mwana wake Yesu Khristu, kuti adzapereke dipo la uchimo wathu ndi kufa m; malo mwathu. “Koma Mulungu atsimikiza kwa ife cikondi cace ca mwini yekha m’menemo, kuti pokhala ife cikhalire ocimwa, Kristu adatifera ife” (Aroma 5:8).

7 Amai kuti akadziwe za chipulumutso chimene chinaperekedwa kwa ife mwa mwana wa Mulungu, Yesu. “Yesu ananena naye, ine ndinenjira, ndi coonadi, ndi moyo. Palibe munthu adza kwa Atate, koma mwa Ine” (Yohane 14:6). “Ndipo iwo anati, Ukhulupirire Ambuye Yesu, ndipo udzapulumuka, iwe ndi apabanja ako” (Machitidwe 16:31).

8 Amai kuti akavomera kuti Yesu anafa pa mtanda chifukwa cha machismo awo, anayikidwa m’manda, ndipo kuti anauka kwa akufa, komanso kuti tsopano ali kumwamba. “pakuti, amene ali yense adzaitana pa dzina la Ambuye adzapulumuka” (Aroma 10:13).

9 Amai achikhrisitu kuti akakondwera podziwa kuti Yesu akuwakonzera malo kumwamba. “M’nyumba ya Atate wanga alimo malo okhalamo ambiri. Ngati sikudali kutero, ndikadakuuzani inu; pakuti ndipita kukukonzera inu malo. Ndipo ngati ndipita kukakonzera inu malo, ndidzabweranso, ndipo ndidzalandira inu kwa Ine ndekha; kuti kumene kuli Ineko, mukakhale inunso. Ndipo kumene ndinkako Ine, mudziwa njira yace” (Yohane 14:2-4).

10 Amai kuti akavomereza kuti iwo ndi ochimwa ndi kutembenuka kuchoka m’njira zawo zochimwa, popempha Mzimu Woyera kuti akakhale mwa iwo ndi kuwaphunzitsa njira za Mulungu. “Lapani, batizidwani yense wa inu m’dzina la Yesu Kristu kuloza ku cikhululukiro ca macimo anu; ndipo mudzalandira mphatso ya Mzimu Woyera” (Machitidwe 2:28).

11 Amai achikhrisitu kuti akazindikira kuti matupi awo ndi pokhalamo pa Mulungu, Mzimu Woyera, ndipo kuti akuyenera kusamalira matupi awo ndi kubweretsa ulemu kwa Mulungu. “Kodi simudziwa kuti muli Kacisi wa Mulungu, ndi kuti Mzimu wa Mulungu agonera mwa inu?” (1 Akorinto 3:16).

12 Amai kuti amvetsetse kuti sangachite kanthu kuti adzipulumutse okha, koma kuti chipulumutso chawo chinabwera mwa chisomo cha Mulungu. (Aefeso 2:8-9).

13 Amai kuti amvetsetse kuti iwo analengedwa kuti “mwa Kristu Yesu, kucita nchito zabwino” (Aefeso 2:10).

14 Amai kuti amvetsetse kufunikira kophunzira zimene Mawu a Mulungu akunena, ndi kusintha malingaliro komanso machitidwe awo molingana ndi Malemba. “Khalani akucita mau, osati akumva okha, ndi kudziyenga nokha” (Yakobo 1:22)

15 Amai kuti akasanthula Mawu a Mulungu ndi kuyamba kumvetsetsa malingaliro komanso zochita za Mulungu.